Phunziro 7: Imvani Izi!

A. Kuzunza Aneneri

1. Kodi Yesu anafotokoza kuti aneneri a Mulungu ankachitiridwa zotani m'mibadwo yosiyanasiyana? Mateyu 5:11-12,23:37
2. Kodi mneneri Mose anachitiridwa nkhanza zotani? Numeri 12:1-2, 14:1-2,10
3. Kodi mneneri Yohane Mbatizi anachitiridwa nkhanza zotani? Marko 6:17-20, 21-29
4. Kodi Yesu, mneneri wamkulu kuposa aneneri onse a Mulungu, anachitiridwa nkhanza zotani? Mateyu 26:67, 27:30-31
5. Tchulani aneneri ena a Mulungu amene anazunzidwa chifukwa cholankhula choonadi chochokera kwa Mulungu?
6. Ngakhale kuti masiku ano mwina tilibe aneneri a Mulungu pakati pathu, kodi tingakhale bwanji olakwa pozunza ena mwa atumiki amene amabweretsa uthenga wa Mulungu?
7. Fotokozani za nthawi imene munachitiridwa nkhanza chifukwa chouza ena choonadi cha Mawu a Mulungu.
8. Kodi tiyenera kuchita chiyani ngati anthu akutichitira nkhanza chifukwa chouza ena choonadi cha Mawu a Mulungu? Mateyu 5:10-12, Luka 6:23

B. Kunyalanyaza Kapena Kuwononga Uthenga wa Mneneri

1. Kodi atsogoleri a Aisrayeli anatani atamva uthenga wouziridwa ndi Mulungu umene mneneri Yeremiya anapereka? Yeremiya 36:20-26
2. Kodi wolemba buku la 2 Mbiri (amene mwina anali Ezara) anafotokoza bwanji mmene Aisrayeli ankalandirira mauthenga a aneneri? 2 Mbiri 36:15-16
3. Kodi atsogoleri a Ayuda anatani atamva uthenga wa ulosi umene Stefano, mdindo wa mpingo, anapereka? Machitidwe 7:54-60
4. Fotokozani za nthawi imene munakana kumvera uthenga wochokera kwa AMBUYE, ngati kuti munatseka makutu anu.

C. Chifundo cha Mulungu kwa Ana Ake Osokera

1. Kodi AMBUYE anachita chiyani pamene Mfumu Yehoyakimu inawononga zolemba za mneneri Yeremiya? Yeremiya 36:27-28
2. Yeremiya 36:32 — Zikuoneka kuti uthenga wa zolembera zachiwiri unawonjezeredwa. Kodi mukuganiza kuti ndi zinthu ziti zimene zinawonjezeredwa mu zolembera zachiwirizi?
3. Kodi chifundo cha Mulungu chinaonekera bwanji pamene analamula aneneri ake kuti alembe mbiri ya mmene Iye ankachitira zinthu ndi anthu, komanso mmene anthuwo ankalandirira mauthenga ake? 1 Akorinto 10:6-10
4. Kodi ndi chilimbikitso chotani chimene mumapeza mulonjezo lolembedwa mu 1 Akorinto 10:13?
5. Werengani pemphero la olemba masalimo Davide lolembedwa mu Masalimo 86:3-5. Kodi ndi malemba ena ati a m'Baibulo amene amatikumbutsa za chifundo cha AMBUYE? 1 Peter 1:3, etc.